Moto Wosatha kwa anthu amene akukana kumumvera Iye.



PHUNZIRO LA 36

1. Pamene Mose ankalankhulana ni Mulungu pamwamba pa phiri la Sinayi, kodi a Isilayeli ankachita chiyani pasi pa phirilo?

-A Isilayeli anapanga mwana wa ng'ombe wa golide ndi kumampembedza.

2. Kodi Mulungu anadziŵa kuti a Isilayeli ankapembedza ng'ombe ya golide?
-Inde.

3. Kodi Mulungu anakwiya ndi a Isilayeli?
-Inde.
-Mulungu anakwiya kwambiri ndi a Isilayeli mwakuti ankafuna kuti aŵawononge iwowo.

4. Kodi chifukwa chiyani Mulungu sanaŵawononge a Isilayeli?
-Chifukwa chakuti Mose anapemphera kwa Mulungu kuti asaŵawononge a Isilayeli.

5. Kodi Mose anamuwuza chiyani Mulungu kuti Iye asaŵawononge a Isilayeli?
-Mose anati kuti ngati Mulungu aŵawononge a Isilayeli, ndiye kuti a Iguputo adzanena kuti Iye anaŵatsogolera kuchokera ku Iguputo ndi cholinga chafuna kuwapha.

-Mose ananenanso kuti, Mulungu anati kuti adzasunga lonjezo lake kwa Abulahamu, Isaki ndi Yakobo lakuti adzakhala ndi ana ambiri amene adzachuruke kwambiri.

6. Kodi Mose anachita chiyani atatsikanso mphiri la Sinayi lija?

-Mose anaŵakwiyira a Isilayeli mwakuti anaponya pasi mapale a miyala a malamulo a Mulungu aja ndipo anasweka.

7. Chifukwa chakuti Mose anaphwanya mapale a miyala, pamene Mulungu analembapo malamulo khumi aja, kodi Mulungu anamuwuza Mose kuti achite chiyani?
-Mulungu anamuwuza Mose kuti asemenso mapale ena atsopano a miyala, ndipo apitenawonso pamwamba pa phiri la Sinayi, pamenepo Mulungu analembanso malamulo ake khumi aja.

8. A Isilayeli anakakhala kuti sanamange kachisiyo ngati m'mene Mulungu anaŵalamulililira, kodi ulemelero wa Mulungu unakabwera mkachisimo?
-Iyayi.

9. Kodi a Isilayeli anakatha kuti adzipita kwa Mulungu mu njira yawoyawo?
-Iyayi.

10. Kodi njira yokhayo, imene a Isilayeli anakamapitira kwa Mulungu inali yiti?
-Ya Mulungu Mwini.

11. Kodi njira ya Mulungu tingayidziŵe bwanji?
-Kudzera M'buku la Mulungu, Bayibulo.

-Mulungu anamusankha Mose kuti aŵatsogolere a Isilayeli pochoka ku Iguputo mu ukapolo.

-Nayenso Mose anali wotumikira wa Mulungu.
-Mulungu akafuna kulankhula ndi a Isilayeli, ankalankhula kupitira mwa Mose.

-Mulungu anamutsogolera Mose kuti adzilankhula zimene



wa basi.

31-Kunena za ana anu amene adzagwidwe, Ine ndidzaŵafikitsa m'dziko limene analikana iwowolo, ndipo lidzakhala kwawo.

32-Inu mudzafera m'chpululu mom'muno."

-Chifukwa chakuti a Isirayeli sanamukhulupilire Mulungu, Yoswa, Kalebe ndi ana awo okha ndi amene adzaloŵe mu dziko la Kanani.

-Chifukwa chakuti a Isirayeli sanamukhulupilire Mulungu, iwowo sadzaloŵa mu dziko la Kanani.

-Chifukwa chakuti a Isirayeli sanamukhulupilire Mulungu, iwowo onse adzafera mu chipululu.

-Mulungu adzapereka chilango cha imfa kwa onse amene akukana kumukhulupilira Iye.

-Ndi chinthu choyipa kwambiri kukana kukhulupilira Mulungu.

-Anthu a m'masiku a Nowa anakana kumumvera Mulungu, ndipo Mulungu anaŵapatsa chilango cha imfa.

-Anthu a m'masiku a Sodomu ndi Gomora anakana kumumvera Mulungu, ndipo Mulungu anaŵapatsa chilango cha imfa.

-Farawo ndi anthu ache a ku Iguputo anakana kumumvera Mulungu, ndipo Mulungu anaŵapatsa chilango cha imfa.

-Mulungu adzapereka chilango cha imfa kwa anthu amene akukana kumumvera Iye.

- Mulungu adzapereka chilango cha imfa ya M'nyanja ya

-Inde.

-Kodi Mulungu ankadziŵa kuti a Isirayeli sankakhulupilira zakuti Mulungu adzasunga malonjezo ache oŵapatsa iwowo dziko la Kanani?
-Inde.

-A Isirayeli sankakhulupilira kuti Mulungu adzasunga malonjezo ache ndikuŵapatsa iwowo dziko la Kanani.

-Ngati sitikukhulupilira mawu a Mulungu ndiye kuti ife tikumutcha Mulungu kuti ndi otani?
-Wa bodza.

-A Isirayeli sankakhulupilira mawu a Mulungu.
-A Isirayeli ankamutcha Mulungu kuti ndi wabodza.

-Apa pali zimene analankhula Mulungu.

Tiyeni tiŵerenge Numeri 14:26-32

26-Ambuye anati kwa Mose ndi Aroni:
27-"Kodi kangati ndiponso mpaka liti, anthu oyipaŵa adzikhala akudandawula mutsutsana ndi ine? Ndatopa ndikumva madandawulo awoŵa!
28-Tsopano kuyankha kwache ndi uku, uŵawuze kuti, "Ine ndikulumbira kuti, pakuti Ine ndi wa moyo, ndidzaŵachitira zimene apemphazo. Ine Ambuye ndalankhura.
29-Iwowo adzafa ndipo mitembo yawo idzabalarika mchipululu muno. Chifukwa chakuti iwowo adandawula motsutsana ndi Ine, palibe mwa iwowo amene waposa zaka makumi aŵiri amene adzaloŵe m'dzikolo.
30-Ine ndinakhazikitsa pangano lakuti iwowo adzakhala kumeneko, koma palibe ndi m'modzi yemwe mwa iwowo amene adzaloŵe kumeneko, koma Kalebe ndi Yos-



Iye ankafuna kuti Moseyo alankhule.

-Mulungu anamutsogolera Mose kulemba zimene Iye ankafuna kuti Moseyo alembe.

-Mose ndi amene analemba mabuku asano oyambirira a m'buku la Mulungu, Bayibulo.

-A Isilayeli anali atachoka ku Iguputo ndipo anali akuyenda mchipululu.

-Mchipululu mulibe njira.
-Mchipululu muli mchenga okhawokha.

-Kodi a Isilayeli ankayidziŵa bwanji njira?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 40:36-37

36-Monse m'mene ankayenda a Isilayeli, mtambo ukanyamuka kuchoka pa kachisi wa Mlungu, nawonso ankawuyamba ulendo;
37-koma ngati mtambowo siwukunyamuka , nawonso sankawuyamba ulendo mpaka pa tsiku limene udzanyamukirelo.

-Mulungu ankaŵatsogolera a Isirayeli ndi mtambo pa nthaŵi ya masana.
-Mulungu ankaŵatsogolera a Isirayeli ndi mtambo wa moto pa nthaŵi ya usiku.

-Mulungu akafuna kuti a Isirayeli ayime, Iye ankawuyimitsa mtambowo.
-Mulungu akafuna kuti a Isirayeli ayende, Iye ankawuyendetsa mtambowo.

-Ngakhale kuti a Isirayeli sankamukhulupilira Mulungu, Iye

anapitirizabe kuŵatsogolera iwowo.

-Mulungu atatha kuŵapatsa malamulo khumi a Isirayeli, ndipo a Isirayeli atatha kumanga kachisi wa Mulungu, Mulungu anawunyamula mtambo uja.

-Kodi Mulungu ankaŵatsogolera a Isirayeli kupita kuti?

-Mulungu ankaŵatsogolera a Isirayeli kupita ku dziko la Kanani, limene analilonjeza Mulungu kwa kholo lawo, Abulahamu.

-A Isirayeli anawutsatira mtambo mpaka anakafika ku malire a dziko la Kanani.

-A Isirayeli atafika ku malire a dziko la Kanani, Mulungu anamuwuza Musa kuti asankhe amuna 12, m'modzi ku mtundu uliwonse pa mitundu 12 ija.

-A Isirayeli asanaloŵe m'dziko la Kanani, Mulungu anafuna kuti anthu 12 aja apite kukulizonda kaye dzikolo.

Tiyeni tiŵerenge Numeri 13:1-2

1-Ambuye anati kwa Mose,
2-"Usankhe munthu m'modzi mwa atsogoleri a fuko lililonse pa mafuko khumi ndi aŵiriwo, ndipo uŵatumize kuti akazonde dziko la Kanani limene ndikuŵapatsa ana a Isirayeli."

-Mose anamumvera Mulungu ndipo anaŵatumiza amuna 12 aja kuti akalizonde dziko la Kanani lija.

Tiyeni tiŵerenge Numeri 13:3



so musaŵawope anthu amene akukhara kumeneko. Tidzaŵagonjetsa iwowo mosavuta. Ambuye ali pamodzi ndi ife ndipo ayigonjetsa milungu imene inkaŵateteza iwowo, chomcho musawope."

-Kalebe ndi Yoswa anaŵapempha a Isirayeli kuti adzimumvera Mulungu.
-Kalebe ndi Yoswa anaŵawuza a Isirayeli kuti Mulungu ndi amene anali ndi mphamvu zambiri ndipo adzatha kuŵagonjetsa anthu amene akukhala mu dziko la Kanani.

-Kodi a Isirayeli anagwirizana nazo zoloŵa m'dziko la Kanani zija?

Tiyeni tiŵerenge Numeri 14:10a

10-Khamu lonse la anthu linkaŵawopsyeza kuti liŵapha poŵagenda ndi miyala.

-A Isirayeli sanafunebe zoloŵa mu dziko la Kanani lija.
-A Isirayeli sanafunebe kumumvera Mulungu.
-A Isirayeli ankafuna kuŵagenda Kalebe ndi Yoswa ndi Mose yemwe ndi miyala.

-Kodi Mulungu ankamva zimene ankalankhula a Isirayelizo?
-Inde.

-Kodi Mulungu anadziŵa kuti a Isirayeli sankafuna kuloŵa mu dziko la Kanani?
-Inde.

-Kodi Mulungu ankadziŵa kuti a Isirayeli sankamukhulupilira kwambiri Mulungu kuti anali ndi mphamvu zambiri mwakuti anakatha kuŵagonjetsa anthu amene ankakhala mu dziko la Kanani?

-Kodi a Isirayeli anaŵakhulupilira amuna khumi amene sankamukhulupilira Mulungu aja kapena anaŵakhulupilira Yoswa ndi Kalebe amene ankamukhulupilira Mulungu aja?

Tiyeni tiŵerenge Numeri 14:1-4

1-A Isirayeli atamva zimene ananena anthu khumi ndi aŵiri amene anakazonda dziko la Kanani aja, anachezera kulira usiku onse.
2-Iwowo anadandawura motsutsana ndi Mose ndi Aroni, ndipo anati kuti, “Kunakakhala kwabwino kufera mu Iguputo mom’muja kapena m’chipululu mom’muno!
3-Kodi chifukwa chiyani Ambuye akutitengera ife mu dziko limeneli? Ife akatipha ku nkhondo, ndipo ana athu ndi akazi athu akaŵagwira. Kodi sizingakhale bwino kuti tibwerere ku Iguputo?”
4-Chomcho anawuzana wina ndi mzache kuti, “Tiyeni tisankhe otitsogolera kuti tidzibwerera ku Iguputo!”

-A Isirayeli anaŵamvera amuna khumi amene sakamumvera Mulungu aja, ndipo sanafune kuti akaloŵe mu dziko la Kanani.

-Kalebe ndi Yoswa analankhulanso kwa a Isirayeli.

Tiyeni tiŵerenge Numeri 14:6-9

6-Yoswa mwana wa Nuni ndi Karebe mwana wa Yefune, aŵiri mwa azondiwo, anang’amba zovara zawo mwa chisoni.
7-Ndipo anati kwa anthu aja, “Dziko limeme ife tanakalizonda, ndi lokongora kwambiri.
8-Ngati Ambuye adzasangalare ndi ife, adzatitengera kumeneko ndi kukalipereka dziko la chumalo ndipo la chondelo kwa ife.
9-Musaŵawukire ndikutsutsana ndi Ambuye ndipo-



3-Mose anaŵamvera Ambuye ndipo anaŵatumiza akuruakuruwo kuchokera mchipululu cha Palana.

-Kodi Mose anaŵawuza chiyani amuna 12 aja asanaŵatumize kukazonda dziko la Kananilo?

Tiyeni tiŵerenge Numeri 13:17-20

17- Pamene Mose ankaŵatumiza azondiwo kuti akazonde dziko la Kanani, anaŵawuza kuti, “Mudzere ku dziko la Negefa mpaka ku dziko la ku mapiri a Kanani.
18-Mukawonetsetse kuti kodi ndi dziko lotani, kodi muli anthu angati amene akukhala m’menemo, ndiponso kodi mphamvu zawo ndi zotani.
19-Mukawonetsetsenso ngati dzikolo lili labwino kapena loyipa, ndiponso kodi anthu ake akukhala m’mizinda yotani. Kapena mizinda yake yili ndi malinga?
20-Mukawonetsetsenso ngati dothi lake lili la nthaka ndiponso ngati dzikolo lili ndi mitengo. Ndiponso musakayiŵale kubweretsa zipatso za kumeneko.”

-Patatha masiku 40, amuna 12 aja anabwerako kokalizonda dziko la Kanani kuja.
-Izi ndi zimene anabwera nazo kuchokera ku dziko limene anakalizonda amuna 12 aja.

Tiyeni tiŵerenge Numeri 13:27-28

27-Azondi aja anati kwa Mose, “Ife taliyendera dzikolo ndipo taliwona kuti ndi lachuma ndipo lili ndi nthaka, izi ndi zina mwa zipatso zake.
28-Koma anthu amene akukhala kumeneko ndi a mphamvu kwambiri, ndiponso mizinda yawo ndi yayikuruyikuru kwambiri ndipo yili ndi malinga ake. Chimene chili choyipa ndi ichi, taziwona zidzukuru za Anaki kumeneko.”

-Dziko la Kanani linali dziko la mkaka ndi uchi.
-Dziko la Kanani linalinso dziko la anthu akuluakulu ndipo a mphamvu kwambiri.
-Mizinda ya ku Kanani inalinso yomangidwa mwangwiro, ndipo inali yozunguliridwa ndi malinga ataliatali.

-Mwa amuna 12 amene anapita kukalizonda dziko la Kanani aja, khumi mwa iwowo samamukhulupilira Mulungu.

-Izi ndi zimene ananena kwa a Isirayeli amuna khumi amene samamukhulupilira Mulungu aja.

Tiyeni tiŵerenge Numeri 13:31-33

31-Koma anthu ena mwa amene anapita nawo, anati kuti, “Iyayi, ife tilibe mphamvu zokaŵayambira iwowo, pakuti anthu ache ndi a mphamvu kuposa ife.”
32-Chomcho iwowo anafalitsa nkhani ya bodza pakati pa a Isirayeli ya dziko limene analiyenderalo. Ankalankhula kuti, “Dzikolo silingabereketse chakudya chokwanira kuŵadyetsa anthu amene akukhala m’menemo. Ndipo anthu onse amene anaŵawona anali ataliatali.
33-Ndiponso tinaŵawona anthu akuluakulu kumeneko, zidzukulu za Anaki. Ife timangowoneka ngati ziwala, umu ndi m’mene timawonekera kwa iwowo.”

-Amuna khumi amene samkamukhulupilira Mulungu aja, ankaŵawopa anthu akuluakulu ndiponso a mphamvu amene ankakhala mu dziko la kanani aja.

-Amuna khumi amene samkamukhulupilira Mulungu aja, sankakhulupilira kuti Mulungu anapereka lonjezo kwa a Isirayeli loŵapatsa dziko la Kanani.

-Amuna khumi amene samkamukhulupilira Mulungu aja, sankakhulupilira kuti Mulungu anali wa mphamvu kwambiri mwakuti anakatha kuŵagonjetsa anthu amene ankakhala mu dziko la Kanani lija.



-Amuna khumi amene samkamukhulupilira Mulungu aja, anaŵawuza a Isirayeli kuti asaloŵe mu dziko la Kanani.

-Mwa amuna 12 aja, panali amuna aŵiri amene ankakhulupilira mwa Mulungu.
-Mayina awo anali Yoswa ndi Kalebe.
-Kodi Yoswa ndi Kalebe anaŵawuza chiyani a Isirayeli?

Tiyeni tiŵerenge Numeri 13:30

30-Koma Kalebe anaŵaletsa kulongolora anthu amene ankadandawula motsutsana ndi Mose aja, ndipo anati kuti, “Tiyeni tikaŵayambe tsopano lino ndipo tikalitenge dzikolo, ife ndi amphamvu kwambiri mwakuti tikalilanda dzikolo.”

-Kalebe ndi Yoswa sankaŵawopa anthu akuluakulu ndiponso a mphamvu amene amkakhala mu dziko la Kanani.

-Kalebe ndi Yoswa ankakhulupilira kuti Mulungu asunga pangano lache ndi kuŵapatsa a Isirayeli dziko la Kanani.

-Kalebe ndi Yoswa ankakhulupilira kuti Mulungu anali ndi mphamvu zambiri mwakuti anakatha kuŵagonjetsa anthu amene ankakhala mu dziko la Kanani.

-Kalebe ndi Yoswa anaŵawuza a Isilayeri kuti iwowo adzimumvera Mulungu ndipo adzaloŵa mu dziko la Kanani.